-Kodi anthu ali ndi mzeru zambiri koposa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi pali chinthu china chilichonse chimene Mulungu sachi-dziwa?
-Palibe.

-Palibe chinthu china chilichonse chimene Mulunu sachidzi-wa.
-Palibe chinthu china chilichonse chimene Mulungu sachimva.

-Mulungu amadziwa china chilichonse cha chinthu china chil-ichonse.

-Ichi ndi chifukwa chake kuli kofunika kwambiri kuti mudzimvera mawu a Mulungu.



PHUNZIRO LA 5

1. Kodi ndi ndani yekha amene analipo pachiyambi?
-Mulungu.

2. Kodi angelo anachokela kuti?
-Analengedwa ndi Mulungu.

3. Kodi Mulungu anaŵalenga angelo ndi minofu, mafupa ndi magazi?
-Iyayi.
-Mulungu anaŵalenga angelo ngati mizimu.

4. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anaŵalenga angelo?
-Kuti adzimukonda Mulungu.
-Kuti adzimumvera Mulungu.
-Kuti adzimutumikira Mulungu.

5. Kodi Mulungu anŵalenga angelo ena abwino ndipo ena oyipa?
-Iyayi.
-Mulungu analenga angelo onse abwino.

6.Kodi Mulungu analenga angelo angati?
-Mulungu analenga angelo ambiri ndipo palibe amene an-gathe kuŵaŵerenga.

7. Pachiyambi, kodi angelo onse amkakhala kuti?
-Kumwamba ndi Mulungu.

8. Kodi ndi ndani amene Mulungu anamulenga ngati wamku-lu wa angelo onse?
-Lusifala.

9. Kodi Mulungu anamulenga Lusifala ali wabwino kapena oyipa?

-Wabwino.
-Mulungu malenga zinthu zabwino zokhazokha.

10. Pachiyambi, kodi chinachitika ndi chiyani kwa Lusifala?
-Lusifala anaziwona mphanvu ndi nzeru zake zambiri, anayamba kunyada ndipo anaganiza zofuna kumulanda udindo Mulungu.

11. Kodi ena anali ndani amene anamutsatila Lusifala pomuwukira Mulungu?
-Angelo ena ambiri.

12. Kodi Mulungu anadziŵa kuti Lusifala wakhoza zofuna kumuwukira Iye?
-Inde.
-Palibe chimene Mulungu sachidziŵa.

13. Kodi pali china chilichonse chimene Mulungu samachiwona, kumva kapena kuchidziŵa?
-Palibe.
-Mulungu amawona,amamva, ndipo amadziŵa china chilichonse.

14. Kodi Mulungu anamulola Lusifala kupitiliza kukhala ndi Iye?
-Iyayi.
-Mulungu anamuchotsa kumwamba Lusifala pamodzi ndi angelo onse amene anamutsatira iye.

15. Kodi Mulungu anakonza malo otani a Lusifala pamodzi ndi angelo onse amene anamutsatira iye ngati chilango chawo?
-Nyanja ya Moto Wosatha.

16. Kodi dzina latsopano la Lusifala ndi ndani?
-Tsopano Lusifala ndi Satana.



-Ngati pachiyambi panali Mulungu yekha, panalibenso wina aliyense kapena china chilichonse chimene chanakamuphunzitsa Mulungu.

-Ndipo Mulungu samafuna wina aliyense kapena china chilichonse kuti chidzimuphunzitsa Iye.
-Kodi chifukwa chiyani Mulungu samafuna wina aliyense kapena china chilichonse kuti chidzimuphunzitsa Iye?

-Mulungu amadziwa zinthu zonse.
-Nzeru za Mulungu zilibe malire.

-Mulungu samafuna kuti munthu wina aliyense kapena chinthu china chilichonse chidzimuphunzitsa.
-Palibe chinthu chimene Mulungu sachidziwa.
-Nzeru za Mulungu ndi zosatha.
-Nzeru za Mulungu zilibe malire.

-Zilibe malire nzeru za Mulungu.
-Ndi zosatha nzeru za Mulungu.

-Mulungu analenga dziko la pansi posagwiritsa ntchito chinthu china chilichonse.

-Kodi pali munthu amene ali ndi mzeru zambiri koposa Mulungu?
-Palibe.

-Kodi Satana ali ndi mzeru zambiri koposa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi ziwanda za Satana zili ndi mzeru zambiri koposa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi anthu ali ndi mphamvu zambiri kuposa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi pali chinthu china chilichose chimene Mulungu sangathe kuchipanga?
-Palibe.

-Mulungu angathe kupanga china chilichose chimene Iye akufuna kuchipanga.
-Mulungu angathe kupanga zinthu zonse zimene Iye akufuna kuzipanga.

-Kodi Mulungu anadziwa bwanji kulenga zinthu zonse popanda kugwiritsa ntchito chinthu china chilichose?

-Kodi pali amene anamuphunzitsa Mulungu kulenga kwa zinthu zonse?

-Azibambo mumawaphunzitsa ana anu amuna kulima kwa chimanga, chifukwa chakuti anawo sadziwa kulima kwa chimangacho.

-Azimayi mumawaphunzitsa ana anu akazi kuphika, chifukwa chakuti ana akaziwo sadziwa kuphikako.

-Kodi pali munthu amene anamuphunzitsa Mulungu kulenga dziko la pansi ndi kumwamba?
-Palibe.

-Kodi chifukwa chiyani palibe amene anamuphunzitsa Mulungu?
-Pachiyambi, panalibe munthu kapena china chilichonse chimene chinakatha kumuphunzitsa Mulungu.
-Zowona, Mulungu safuna kuphunzitsidwa ndi wina aliyense kapena china chilichonse.



17. Kodi dzina lakuti Satana likutathawuza chiyani?
-Dzina lakuti Satana likutanthawuza kuti m'dani.

18. Kodi angelo amene anamutsatila Satana amatchedwa ndani tsopano?
-Ziwanda.

19. Kodi satana ndi ziwanda zake akukhala kuti tsopano?
-Satana ndi ziwanda zake akukhala pa dziko la pasi tsopano.

20. Kodi satana ndi ziwanda zake amapanga chiyani tsopano?
-Amalimbana ndi ntchito ya mulungu usiku ndi usana.

-Tiyeni tiŵerengenso mawu oyamba a M'buku la  Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:1

1-Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko la pasi.

-Kodi chiyambi ndi chiyani?

-Pachiyambi ndi nthaŵi yayitali yapitayo yimene Mulungu analenga chinthu china chilichose.

-Chinthu china chilichose chimene chili pa dziko la pasi chinalengedwa ndi Mulungu pachiyambi.

-Kodi pa dziko la pasi panali chiyani Mulungu asanalenge chinthu china chilichose?
-Palibe.

-Kodi nanga ngati panalibe chinthu china chilichose pa dziko la pasi , Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga zinthu

zonse?

-Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga kumwamba ndi dziko la pasi ?
-Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi?

-Kodi kunakakhala kulibe mitengo, amuna anakatha kumamanga nyumba?
-Iyayi.

-Kodi amunanu munakatha kumamanga nyumba osagwiritsira tchito chinthu china chilichose?
-Iyayi.

-Kodi kunakakhala kulibe dothi, akazi  anakatha kumawumba mbiya?
-Iyayi.

-Kodi akazinu munakatha kumawumba mbiya popanda kugwiritsa ntchito chinthu china chilichose?
-Iyayi.

-Kodi kunakakhala kuti kulibe bango, ana anakatha kumapanga chidole?
-Iyayi.

-Kodi ananu munakatha kumapanga zidole popanda kugwiritsa ntchito chinthu china chilichose?
-Iyayi.

-Ngati kunalibe chinthu china chilichose pa dziko la pasi, kodi nanga Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga chinthu china chilichose?
-Palibe.



-Kodi nanga Mulungu analenga bwanji dziko la pasi?

-Mulungu analenga dziko la pasi posagwiritsa nchito chinthu china chilichose.

-Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Mpulumutsi), ndi Mulungu Mzimu oyera analenga zithu zose pasagwiritsa ntchito chinthu china chilichose.

-Kodi Mulungu anatha bwanji kulenga kumwamba ndi dziko la pasi posagwiritsa ntchito chinthu china chilichose?

-Kodi Mulungu anatha bwanji kulenga zinthu zonsezi popanda kugwiritsa nthito chinthu china chilichose?

-Mulungu ndi wamphamvu zonse.
-Mphamvu ya Mulungu  siyitha.
-Mphamvu ya Mulungu ndi yampaka kalekale.

-Palibe chimene Mulungu sangachichite.
-Mulungu akhoza kuchita zinthu zonse.

-Mphamvu ya Mulungu yilibe malile.
-Mphamvu ya Mulungu siyitha.

-Mulungu analenga dziko lose la pasi popanda kugwiritsa ntchito chinthu china chilichose.

-Kodi pali amene ali ndi mphamvu zambiri kuposa Mulungu?
-Palibe.
-Kodi Satana ali ndi mphamvu kwambiri kuposa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi ziwanda za Satana zili ndi mphmvu zambiri kuposa Mulungu?
-Iyayi.